

Kufalitsa nkhani:
Kugwiritsa ntchito Nyuzipepa
(Media Press)



TIMVERENI

Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera M'maphunziro, Zaluso ndi
Njira Zofalitsira Mauthenga



TIMVERENI

Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

**Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera
M'maphunziro, Zaluso ndi Njira zofalitsira
Mauthenga**

**Kufalitsa Nkhani: Kugwiritsa
Ntchito Nyuzipepalala**

Kabukuka ndi kamodzi ka mabuku a maphunziro a TIMVERENI Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana. TIMVERENI ndi maphunziro olimbikitsa ufulu wa ana kudzera m'maphunziro, zaluso ndi njira zina zofalitsira mauthenga. Mabukuwa analembedwa mu chaka cha 2011 ngati mbali imodzi ya pulojekiti ya IPEC/ILO ndi chithandizo chochokera ku boma la Italy.

IPEC/ILO ikulimbikitsa kuti mabukuwa athe kuyikidwa mu zilankhulo zosiyanasiyana komanso kusindikizidwanso kuti ntchito yothetsa nkhanza kwa ana ipite patsogolo. Ngati mwatanthauzira bukuli mu chinenero china kapena kusinthako mbali ina ya mabukuwa, kumbukirani kunena komwe mwatenga uthengawo ndiponso mutumizireko a ILO/IPEC mabukuwo kapena mbali yomwe mwasintha.

TIMVERENI – Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana. Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera M'maphunziro, Zaluso ndi Njira Zina Zofalitsira Mauthenga, Ntchito Yolimbana ndi Khalidwe Lolemba Ntchito Ana pa dziko lonse, International Programme on the Elimination of Child Labour (IPEC), International Labour Organisation (ILO), Geneva, 2011.

ISBN N. 92-2-113 240-4

Mungathe kudziwa zambiri za TIMVERENI kuchokera ku:
International Programme on the Elimination of Child Labour (IPEC)
International Labour Organisation (ILO)

4, Route des Morillons, CH-1211 Geneva 22, Switzerland
Telephone: +41 22 799 77 47
Fax: +41 22 799 81 81
Email: childlabour@ilo.org
Web site: www.ilo.org/scream

Cholinga: Kulimbikitsa kukumana ndi ofalitsa nkhani ndicholinga chobweretsa chidwi cha anthu ku nkhani ya m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana. Kumvetsa momwe ofalitsa nkhani amagwirira ntchito. Kuphunzira kulemba kalata ya chidziwitso ndi kuwonetsetsa kuti yasindikizidwa mu nyuzipepalala.



Phindu: Anthu akumudzi adzakhala ozindikira ndi kuyamba kuchitapo kanthu komanso kupititsa patsogolo mauthenga okhudza nkhani yogwiritsa ntchito ana ang'ono.

Nthawi:

Maphunziro awiri muchigawo chimodzi ndi limodzi mu zigawo ziwiri

Chilimbikitso

Chida chofunika kwambiri pa nkondo yolimbana ndi m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana ndi kugwiritsa ntchito ofalitsa nkhani ndi nyuzipepalala. Masiku ano, pamene nkhani zikuyenda mofulumira padziko onse, ndikofunika kwambiri kugwiritsa ntchito ofalitsa nkhani ndi nyuzipepalala polimbikitsa chidziwitso cha anthu pa nkhani yogwiritsa ntchito ana.



Taphatikiza zigawo ziwiri zofalitsa nkhani: choyamba chikufotokoza zolemba; nyuzipepalala ndi magazini (magazine) pamene china chikufotokoza za wailesi ndi television. Zigawo zonsezi zikufotokoza momwe achinyamata angagwiritsire ntchito ofalitsa nkhani ndi nyuzipepalala podziwitsa anthu a mudela lawo pa zomwe akuchita ndi momwe anthuwa angathandizire.

Maphunzirowa amapereka mpata kwa achinyamata kuti agwiritse ntchito maluso omwe iwo aphunzira mu ma gawo ena a m'mbuyo.



Chidziwitso

Ndibwino kugwiritsa ntchito chigawo cha Kafukufuku ndi Nkhani musanagwiritse ntchito chigawo ichi.

Achinyamatawa adule zopezeka mu nyuzi ndi magari zokhudza kulemba ana ntchito ndi nkhani zina za ufulu wa anthu. Pounika mozama zodulidwazi gulu lanu lidzatha kuona momwemutu wa nkhani ogwira mtima, komanso kalembedwe kabwino kamakhalira

Achinyamata akhonza kufotokoza zakuipa kogwiritsa ntchito ana munjira yoti ana anzawo padziko lonse athe kumva. Pogwiritsa ntchito ofalitsa nkhani ndi nyuzipepala akhonza kulongosola nkhani, kupempha chithandizo, komanso kupempha anthu ena kuti achitepo kanthu. Chigawo ichi chikulumikizana bwino ndi zigawo zina monga Kulemba Nkhani Mopeka. Luso lolemba nkhani mopeka lidzawathandiza polemba makalata achidziwitso.

Kawirikawiri achinyamata sapatsidwa mpata wotengako mbali pa zinthu zikuluzikulu. Chigawo ichi chiwapatsa mpata kuti owonetse zimene angathe kuchita. Kugwira ntchito ndi ofalitsa nkhani ndi nyuzipepala kukusanduka chinthu chofunika m'moyo wazachuma wa masiku ano ndipo nkhani zikutenga malo akulu pa miyoyo anthu. Luso ili lidzawathandiza pamoyo wawo wapatsogolo; ku sukulu komanso kuntchito.

Chigawo ichi chikuthandizani kuona ndikuyesa luso laachinyamata amene mukugwira nawo ntchito; zidzakusonyezani luso la utsogoleri, lolumikizana ndi ena komanso lakutha kulingalira za nkhwana za anthu ena zimene achinyamatawa ali nazo.

Kukonzekera

Nkhani imakambika bwino pamene ikuchitika. Lankhulani za pulojekiti yanu pamene zinthu zikuchitika osati patapita nthawi zinthuzi zitatha. Ngati mphunzitsi mukuyenera kusankha nthawi yoyenera kugwiritsa ntchito chigawo ichi.

Inu ndi gulu lanu muyenera kukumana ndi olemba nkhani ndi akonzi anyuzupepala musanapereke kalata yanu yachidziwitso. Akonzi ayenera kudziwitsidwa nthawi isanafike ndipo ayenera adziwe kuti kalatayi idzakamba zachiyani. Ayenera kuti akonzekere bwino za momwe nyuzipepalala yawo yotsatira idzakhalire. Pokumana nawo mudzatha kudziwa ngati ndikoyenera kupereke kalata yanu yachidziwitso pa nthawiyi kapena pa nthawi ina.

Sibwino kulemba kalata yachidziwitso ndikuitumiza ku nyuzipepala mukudziwa kuti sidzasindikizidwa- izi zikhonza kukhumudwitsa gulu lanu.

Nkhani imene mwalemba imakhala ndizotsatira zabwino ngati mwaikamo zithunzi zofotokozera. Pamene mukulankhula ndi atolankhani apempheni kuti akuuzeni nthawi ndi malo abwion ojambulitsira zithunzi, anthu akunja oti adzalankhule kapena maguluoti adzasangalatse anthu ndi zina zotere. Onetsetsani kuti ojambulawo akudziwa bwino za nthawi ndi malo kuti asadzataye nthawi kukudikilirani- amakhala otanganidwa kwambiri.



Ngati muli ndi anzanu amene anagwirapo ntchitoyi ndipo ndiwokonzeka kukuthandizani, apempheni kuti atero. Mwinanso mukhonza kukhala kuti mukudziwa wina wake, likhonza kukhala kholo la m'modzi mwa achinyamata anu, amene amagwira ntchito yofalitsa mawu kapena anagwirako ntchitoyi-mupempheni munthu otereyu kuti akuthandizeni.

Kupeza Thandizo

Zikhonzanso kutheka kuti nyuzipepalala ya mudela lanu ingatumize m'modzi mwa ogwira ntchito awo kuti adzakuthandizeni pa ntchitoyi. Nthawi zinanso akhonza kungobwera ndikudzalankhula nanu pa za ntchito ya atolankhani ndi momwe mungapangire kuti nkhanu yanu isindikizidwe. Achinyamata amakhala ndi chidwi kwambiri pofuna kudziwa momwe ofalitsa nkhanu ndi nyuzipepalala amagwirira ntchito makamaka chifukwa chakuti amamvera wailesi ndi kuonera television nthawi yambiri. Komanso pogwiritsa ntchito chithandizo cha bungwe lofalitsa mau ndi nyuzipepalala ya mudela lanu, mumapangitsa bungweli kuti lizindikire zimene mukuchita ndikutsekula njira yakuti nkhanu yanu idzasindikizidwe komanso kuti mudzapatsidwe mpata oyankha mafunso pa wailesi kapena pa television. Kutu mwayi oterewu upezeke pamafunika kuti mupeze upangiri wa katswiri pofalitsa nkhanu. Ngatisimukudziwawina aliyense wa akatswiriwa, mukhonza kuyang'ana maina a anthu otere mu nyuzipepalala, kapena mu buku la maina a telefoni. Mukhonza kuwafunsa ngati angathe kukuthandizani pantchitoyi mwaulele.

Zofunikira



- Pepala ndi zolemba.
- Bolodi kapena mapepala akuluakulu olembapo pophunzitsa.
- Telefoni ndi yofunikanso kwambiri ngati inapezeke.



Kuyamba

Momwe mungayambire kugwiritsa ntchito chigawo ichi zidalira pa zinthu zingapo zosiyanasiyana monga:



- Ngati mwatha kuitanitsa odzalankhula ochokera ku nyumba zofalitsa mau kapena ayi.
- Ngati muli ndi nzanu, m'phunzitsi wina kapena munthu wina amene azikuthandizani pa chigawo ichi.
- Ngati muchite zonse za mu chigawochi nokha.

Mulimonse momwe zingakhalire, njira imene yafotokozedwa m'musiyi yayenera kukhala yokwanira kukuthandizani kuchita zonse za muchigawochi pa nokha ngakhal kuti simunagwireko ntchitoyi.

Kukonza gulu

Kupambana kwa zochitika za mu chigawochi kudzatengera chidwi chomwe gulu lanu lingawonetse pa ntchitoyi. Adzayenera kulemba kalata yachidziwitso ndipo izi zingachitike bwino ngati achinyamatawa atakhala mu magulu ang'ono-ang'ono a anthu awiri kapena anayi. Zochitikazi zidzathandiza kuti achinyamatawa asakhale ndi mantha muzochitika zawo makamaka pokumana ndi atolankhani.

Ngati mukupanga chigawo ichi mutatha kuchita chigawo cholembe nkhani za mwamsangulutso, (Creative Art) muyenera kukhala mutapeza anthu odziwa bwino kugwiritsa ntchito mawu. Onetsetsani kuti anthu oterewa asakhale mu gulu

limodzi, koma kuti apatulidwa kukhala mu magulu angapo ndi cholinga chakuti luso lawo lithandize anzawo. Akhonzanso kukhala atsogoleri amagulu awo ang'oanoang'ono, chimene chikhonza kukhala chothandiza kwa inu.

Kukonzekera zochita

Phunziro limodzi

Ngakhale kuti masiku ano, sikovuta kutumiza uthenga, sitiyanera kuyiwala kufunika kwa mau olembedwa. Kalata yachidziwitso yolembedwa bwino komanso yopita kwa anthu oyenera, ndiyomveka bwino, ikhonza kukhala njira yamphamvu yofalitsira uthenga wa ntchito yanu yothandiza kuthetsa m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana.

Zinthu zingakhale bwino ngati mwakwanitsa kuitanitsa odzalankhula ochokera ku nyumba yofalitsa nkhani. Mlendo yu akhale oyamba kulankhula kwa gululi musanayambe kuphunzitsa. Onetsetsani kuti pakhale chigawo cha mafunso ndi mayankho akatha kulankhula. Nthawi zina achinyamata amakayikayika kuti afunse mafunso ngakhale atakhala nawo ambiri. Choncho yambitsani zonse pofunsa mafunso angapo inu eni. Izi zimachotsa mantha achinyamatawa ndipo akhonza kukhala omasuka kwambiri kuti afunse mafunso awo.

Lembani ndikutumiza kalata yothokoza kwa olankhulayo pamapeto pa ulendo wake. Zinthu zazing'ono ngati izi zimayamikidwa ndipo zimathandiza kuti munthuyu adzamasuke ndikuthandizanso mtsogolo.

Gulu lisakhale ndi nkawa ngati simunathe kupeza mlendo odzalankhula chifukwa nyumba zolembe nyuzi, ngakhale zazing'ono za mu dela lanu zimakhala zotanganidwa kwambiri. Atolankhani awo ayenera kuti amapita kutali kwa nthawi yaitali kukasaka nkhani, kufufuza mphekesera zomwe amva, kufunsa mafunso, kuongolera zina ndi zina kuphatikizapo kujambula zithunzi. Kenako amayenera kukhala mu ofesi mwawo kuti alembe nkhani zawo. Amakhala ndi zochita zambiri pokonzekera kutulutsa nyuzi ya sabata iliyonse. Nthawi yawo ndiyamtengo wapatali kwambiri. Choncho njira yabwino kwambiri yoti muwakope ndikugwiliratu ntchito zina m'malo mwawo. Mungathe kutero polemberatu kalata yachidziwitso imene angathe kungoisindikiza yonse mu nyuzi zawo ngati kutakhala koyenera kutero kapena ngati atasowa nthawi yofufuzira zambiri.




Gawo loyamba la Zochitika: Kulemba kalata yachidziwitso yopita ku nyuzipepala mongofanizira

Phunziro limodzi la magawo awiri

Yambani ndi gulu lonse pamodzi. Lembani pa bolodi zinthu zoyambilira komazofunika k w a m b i r i polemba kalata yachidziwitso. Lembani ziganizo zimene zasindikizidwa mizere kungsi kwawo ndipo fotokozani zambiri pa chiganizo chilichonse pamene mukupitilira kulemba.

- **Kodi nkhani ndi chiyani?** Kuti ikhale nkhani yogwira mtima, kalata yanu iyenera kufotokoza nkhani yabwino. Zimathandiza ngati mwayilemba ngati nkhani ya msangulutso fotokozani zinthu zomwe zili zatsopano, zosiyana ndi zinthu zina mu pulojekiti yanu.
- **Lembani ziganizo zazifupi komanso zosavuta.** Nthawi imene owerenga ambiri amakhala ndi chidwi powerenga ndiyaifupi kwambiri mwakuti ziganizo zitalizitali zikhonza kuwagwetsa ulesi komanso kuwasokoneza.
- **Fotokozani mutu wa nkhani yanu mu ndime yoyamba ya kalata yanu.** Fotokozani nkhani yanu muziganizo zisanu zoyamba pogwiritsa ntchito mafunso oti: Ndani? Chiyani? Liti? Kuti? Chifukwa chiyani?



- **Gwirani mau omwe anthu alankhula.** Kubwereza mau amene munthu analankhula kumasangalatsa owerenga. Lolani kuti anthu alankhule mosazimbayitsa pa za nkhani ya m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana kapena za pulojekiti yanu. Ngati mulibe mau enieni amene wina analankhula, tengani zimene mukuzidziwa kuti ndizoonansipo funsani munthu wina ngati angalore kuti awa akhale ngati mau ake-(koma musamale pochita izi ndipo onetsetsani kuti munthu amene watchulidwa anafunsidwa).
- **Yang'anani mutu wankhani umene udzakhala ndi chikoka.** Mutu waukulu wa nkhani yanu uyenera kugwira chidwi cha owerenga ndipo ndi gawo lofunikira kwambiri mu kalata iliyonse yopita kunyumba yofalitsa mau. Mitu yaying'onoying'ono mkati mwakalata imathandiza kuchepetsa chipwilikiti cha maganizo mu ndime imodzi.
- **Pewani kugwiritsa ntchito mau ozama omwe amagwiritsa ntchito akatswiri pa ntchito yawo kapena mau achinyamata.** Kalata yanu iyenera kukhala yolembedwa bwino ndipo zons zidzikhala mu m'ndandanda wake. Kugwiritsa ntchito mau omwe amagwiritsa ntchito akatswiri pa ntchito yawo kapena mau a achinyamata kukhonza kuchotsa chidwi cha anthu ena.
- **Onetsetsani kuti kalata yanu ndi yayifupi.** Onetsetsani kuti kalata yanu ndiyomveka bwino lomwe, ndiyosakamba mozungulira. Dulani zina zosayenera ndipo lunjikani pa nkhani imene mukufuna kuti anthu amve. Akonzi ena a nyuzi sakhala ndi chidwi ndi kalata yopita ku nyumba yofalitsa mau yomwe ili ndi masamba oposa limodzi. Ndi zoonansipo kuti kulemba zonse zomwe mumafuna patsamba limodzi ndi kovuta, komabe sankhani njira yabwino yolembera nkhani yanu ndikusankha zokhazo zimene zili zofunika kwambiri.
- **Auzeni owerenga kuti inu ndinu ndani.** Pamwamba pa kalata yanu kapena pa tsamba loyambilira lolongosola za kalatayi, muyenera kuyika mau pang'ono kufotokoza kuti inu ndinu ndani ndiponso dzina la gulu lanu.
- **Apatseni ofalitsa nkhani njira yapafupi yoti athe kukupezani.** Ndikoyenera kuti atolankhani apeze munthu oti akhonza kumulankhula kapena kukumana naye kuti amufunse zina ndi zina za kalata yanu, kukonza naye nthawi ndi malo okajambulira zithunzi ndi zina zotere. Muwapatse munthu m'modzi amene adzipanga naye izi kuopa kuti angamataye nthawi posaka anthu osiyanasiyana: akhonza kukhumudwa mwamsanga ndipo mukhonza kutaya mwayi wanu oti nkhani yanu isindikizidwe. Aloleni achinyamatawa kuti afunse mafunso pamene mukuwerenga nawo limodzi izi pa bolodi. Onetsetsani kuti amva mfundo zonse zofunikira ndi zinthu zoyenera kuchita polemba makalata opita ku nyumba zofalitsa nkhani.

Afunseni mafunso kuti muonetsetse kuti amva. Kokani chidwi chawo poonetsetsa kuti mukusakaniza mafunso ndi zimene mukufotokoza komanso zitsanzo.



Kukonzekera Zochitika

Cholinga ndi chakuti timagulu ting'onoting'ono tikhale pamodzi ndikutulutsa makalata awo opita ku nyumba zofalitsira mau. Cholinga sichakuti atulutse kalata yothyakuka bwino kwambiri yomwe ikhonza kutumizidwa ku nyumba yafalitsa mau panthawi iyi. Mwina izi zingakhale zovuta kukwaniritsa pa nthawi yoyamba, ngakhale kuti ndizotheka kuti magulu ena akhonza kukudabwitsani. Cholinga ndikuwathetsa mantha achinyamatawa pa nkhani yolembe ndipo kuchokera apa mukhonza kupitilira kulemba kalata yomaliza pamodzi (onani Gawo Lachiwiri la Zochitika m'musimu).



Kuti aliyense akakhale omasuka mu magulu ang'ono ang'ono, muyenera kukambirana kaye mitu yonse ndi gulu lonse pamodzi (brainstorming). Aliyense apatsidwe mpata onena maganizo ake pa momwe akuyionera nkhani. Cholinga ndichakuti mupeze mutu wa nkhani umene ukhonza kukhala ogwira mtima. Mutu wabwino umapangitsa akonzi, atolankhani ndiponso owerenga kuti athe kuona mutuwu msanga ndikukhala ndi chidwi chofuna kuwerenga nkhani yonse. Ngati muli ndizochitika zimene mwakonzana mtsogolo, kapena zimene zangochitika kumene, mutu wa nkhani uyenera kuonetsa izi. Mukhonza kukonzana mutuwu kuti utukule pulojekiti yonse. Auzeni mamembala a gulu lanu kuti anene mokweza maganizo aliwonse amene angakhale nawo. Aloleni kuti achite izi mosaganizira mozama kwambiri. Lembani pa bolodi maganizo osiyanasiyana amene aperekedwa-ngakhale amene akuoneka ngati opanda ntchito kapena osagwirizana ndi mutu wa nkhani. Kulimbikitsa achinyamatawa kukhala ochenjera poganiza kumawapangitsa kuti akhale ndi chidwi chobweretsa maganizo amene ali ochokera kwa iwo eni ndipo zimawapatsa mwayi oti alembe zimene anthu ambiri adzazikonda. Thetsani gawo limeneli pakatha mphindi zisanu kapena khumi. Kenako lifunsemi gulu kuti lisankhe mwanjira yovota maganizo amene likuona kuti ndioposa onse- mukhonzanso kubweretsa

Pamene mutu wa nkhani wasankhidwa, ulembeni pa bolodi ndipo funsani gulu lililonse kuti lilemba kalata yachidziwitso kuchokera pa mutuwu. Apatseni zotsogolera izi:

- Kuti kalatayo isapitirire mau 250, zimene zikhonza kukhala tsamba limodzi la A4.
- Pakhale ndime yotsogolera nkhani ya mizere yasaposeka isanu imene ifotokoze mfundo yaikulu ya kalatayi pogwiritsa ntchito mafunso oti: Ndani?, Chiyani?, Kuti?, Liti?, Chifukwa chiyani?

- Payenera kukhala mutu waung'ono (wothandizira) osachepera umodzi mu kalatayi.
- Kuti ayenera kugwira mau osachepera a munthu m'modzi, amene akhonza kukhala ochokera kwa m'phunzitsi kapena wina wake wa mugululi.
- Kuti muyenera kukhala “nkhani” mu kalatayi osangoikamo zinthu zomwe ndizoonza zongophatikizidwa ndi mawu ndi ziganizo.

Apatseni maguluwa nthawi yaitali kuti alembe makalata awo; mphindi makumi atatu kapena anayi zikhonza kukhala zokwanira. Onetsetsani kuti zonse zikuyenda bwino pozongulira zongulira m'maguluwa. Khalani kwa kanthawi pang'ono ndi gulu ngati mutaona kuti zikuwavuta kapena ali ndi vuto. Apatseni maganizo angapo pa zimene angaonjezere mu kalata yawo. Kawirikawiri ziganizo zoyambilira ndi zimene zimakhala zovuta kwambiri. Alimbikitseni kuti agwiritse ntchito njira ya: Ndani?, Chiyani?, Kuti?, Liti? ndi Chifukwa chiyani?, popeza izi zidzawathandiza kuyamba ntchito ina iliyonse yolembe powakakamiza kuyankha mafunsowa.

Ntchitoyi ingakhale yosavuta kwambiri ngati gulu lililonse li khala ndi anthu omwe ali ndi luso la kulemba. Mau 250 ndi osavuta kukwanitsa ndipo achinyamata ambiri akhonza kukwanitsa. Atsimikizireni kuti pa nthawi iyi simukuyang'ana kwambiri za ubwino wa zimene alembe. Cholinga chachikulu ndi chakuti gulu lililonse lilemba kenekake ndikutsimikiza kuti akhonza kutero. Yesetsani kuonetsetsa kuti aliyense akutengako mbali pogwira ntchitoyi ndipo kuti simunthu m'modzi amene akulemba. Sungani nthawi imene munawapatsa ndipo onetsetsani kuti gulu lililonse lamaliza munthawi yomwe lapatsidwa. Muyenera kuletsa zolembazi ngati nthawi imene inaperekedwa yatha ngakhale kuti sialiyense amene wamaliza. Uzani gulu kuti lisankhe oliyimilira kuti awerenge kalata yawo. Ngati mukuona kuti mpikisano ukhonza kulimbikitsa chidwi cha gulu lanu, mukhonza kupereka mphotho kwa ntchito imene yatsilizidwa bwino kuposa zina zonse.

Zowonjezera zoyamba (Annex 1) ndi nkhani imene inalembedwa ndi atsikana awiri ang'onoang'ono amene anagwira nawo ntchito yoyeserera ya zigawo izi mu dziko la Ireland m'chaka cha 2001. Nkhaniyi anayisindikiza mu **kalata ya nkhani (newsletter)** ya mudera lawo ndipo ikhonza kukuthandizani inu ndi gulu lanu pochita ntchitoyi. Ndinkhani yooneka ngati ikufotokoza zinthu osakhala ngati kalata yachidziwitso koma inali ntchito yopanga okha.



Gawo lachiwiri la zochitika: Kulemba kalata yenicheni yopita ku Nyuzipepala

Phunziro limodzi la magawo awiri

Cholinga cha ntchito iyi ndikulemba kalata yachidziwitso ndi holinga chakuti ikasindikizidwe mu zowerengedwa zina zilizonse.

Musanapite ku ndime yomaliza yolembe kalata yachidziwitso yomwe yakonzedwa bwino lomwe kuti ikasindikizidwe, muyenera kuyamba mwakambirana momwe mungakumanirane ndi ofalitsa nkhani amene mukufuna kuti akasindikize kalata yanu. Mukhonza kusankha nyumba zoposera imodzi zosindikiza nyuzi za mudera lanu komanso mwina mungathe kulingalira zosindikizitsa kalata yanu mu nyuzi kapena magazini (magazine) ya dziko lonse. Komabe kuti gulu lanu lipindule, komanso pofuna kulimbikitsa kudzidalira, muyambe ndi nyumba imodzi kapena ziwiri zosindikiza nyuzi za mu dera lanu.

Mukatero mukhonza kukhala ndi mwayi waukulu wakuti nkhani yanu isindikizidwe.



Iyi ikhonza kukhala nthawi yoitanitsa thandizo lochokera kunja (monga tanena kale). Ndikofunika kwambiri kukumana ndi aliyense amene angapangitse kuti mwayi woti nkhani yanu isindikizidwe uchuluke. Lipangeni gulu lanu kuti litenge mbali pokumana ndi mkozi kapena mtolankhani. Auzeni kuti asankhe owayimilira pokumana ndi munthuyu ndikuti alembe zonse zomudziwitsa zimene mukufuna kuchita. Gulu lonse litenge mbali popereka maganizo pa zomwe owayimilirawa ayenera kunena pa za kalata imene ili pafupi kutulutsidwa. Fufuzani, nthawi imene ikhonza kukhala yabwino kukumana ndi mkonzi; mwachitsanzo nyuzi papela zambiri zamudera limene mukukhala zimatuluka kamodzi pa sabata, choncho ndi chinthu chothandiza kumuyimbira telefoni mkonzi kutatsala tsiku limodzi kuti nyuzi yake ikasindikizidwe. Muyenera kumuyimbira telefoni mkonziyu, patsiku lomwe nyuzi ikusindikizidwa kapena pakatha tsiku limodzi chisindikizire nyuzi chifukwa pa nthawi sakhala ndi zochita zambiri mu ofesi.

Zinthu zofunika kuti zifufuzidwe ndi monga kudziwa chidwi chimene mkozi ali nacho potulutsa nkhani yokhudzana ndi polojekiti yanu, ndipo kuti akuuzeni nthawi yotsekera kulandira kalatayi. Komanso mkonziyu afunsidwe ngati zithunzi ndizoyenera pofuna kufotokozera bwino nkhanayi ndipo maganizo aperekedwe pa zamomwe ojambula zithunzi wa nyuzi pepalayi angajambulire zithunzizo. Mkonziyu

akhonzanso kukuuzani momveka bwino kutalika koyenera kwa nkhani yanu. Kalata wamba yopita ku nyumba yofalitsa mau iyenera kukhala ya mau 500 (pokhapokhapo ngati mkonzi wakuuzani zosiyana ndi izi), ndipo ngati ndikotheka ikhale yomwe gulu linasankha pa makalata onse omwe analembedwa ndi magulu ang'onoang'ono).

Nkutheka kuti ena mwa makalata amene magulu ang'onoang'ono aja analemba ndi abwinonso kwambiri, chimene chingapangitse kuti ntchito iyi ikhale yosavuta. Kutenga gawo kwanu pachigawo ichi kukhonzana kukhala kofunikira zedi. Makamaka muyenera kuthandiza posankha, kudula ndi "kukonza" zimene makalata a magulu ang'onoang'ono analemba ndikuzipanga kukhala makalata omveka bwino. Muyenera kuti pa nthawiyi mwamva bwinolomwe zimene magulu ang'onoang'ono analemba ndipo mwina munalembedwa zinthu zina zofunika pa zabwino zimene magulu ena analemba. Lankhulani ndi gulu lonse powafunsa kuti chofunika kwambiri kuti chilembedwe kalatayo ndi chiyani. Kodi mutu waukulu umene mukufuna kuti amve ndi uti? Pa nthawi iyi mukhonzana kumangodula zigawo zina ndikuphatikiza pa zigawo zinzake pofuna kuyamba kulemba kalata yanu yomaliza mwatsatanetsatane.



Mwina pangafunike kuonjezera mau ena pokonza kalatayi ndi cholinga chakuti nkhani ilumikizidwe bwino. Izi zikhonzana kuchitika pa bolodi kapena pa mapepala olembapo pophonzitsa (flipchart paper), kapenanso pomufunsa wina kuti alembe zonse zimene mwakambirana kwatsopano. Njira yabwino kwambiri ndikudula ndi kuphatikiza magawo ena ochokera muzigawo za makalata osiyanasiyana. Mukatero sankhani malo ofunika kukonza kuti maganizo anu amveke bwino. Gwirani ntchito ndi gulu lonse ndipo pangani izi kuti zichitike achinyamatawa akusangalala.

Pamene ndondomeko yamau ofunika kulemba yapangidwa, iwunikeninso kachiwiri kuti ikhale yomveka bwino. Mukatenga kalata imene mwalemba komalizirayi, liuzeni gulu lanu kuti lilembe ndime yotsekulira pofunsa mafunso aja oti: ndani? Chiyani? Kutu? Liti? Ndi chifukwa chiyani? Pomaliza yang'ananinso mutu wa nkhani yanu. Dzifunseni mafunso ngati mitu yonse ndiyonera. Ngati mwamaliza kulemba kalata yanu, iwerengeninso kwa gulu lonse ndipo muone ngati palibe maganizo ena atsopano ofuna kukonzanso mutuwu. Ndizotheka kuti maganizo ena akhonza kuperekedwa kuchokera ku kalata yatsopanoyi. Kenako mupemphe m'modzi amene angadzipereke kuti alembe kalata yomaliza polemba ndi manja mwadongosolo kwambiri kapena poyilemba pa kompyutala (**computer**), ngati ndikotheka akupatseni zimene walembazo.

Malangizo

Ndikoyenera kwambiri kuti mupereke kalata yanu nthawi imene mwapatsidwa isanathe. Tsatirani zomwe nyumba yosindikiza nyuzi ya mu dera lanu ikufuna, monga nthawi yotumizira kalata yanu kwa mkozi. Kaperekeni kalata yanu kwa munthu woyenera nthawi yotsekera isanakwane. Fufuzani nthawi yotseka popereka kalatayi pamene mukuyimba telefoni ku ofesi ya olemba nyuzipepala.

Pamene mwatha kulemba kalata yomaliza, thandizani gulu lanu pokumana ndi olemba nyuzi a mu dera lanu kuti atumize kalatayi ndipo muonenso bwino chikonzero chimene chinapangidwa pa nkhani yojambula zithunzi. Kutu mutsimikize kuti kalata iliyonse yopita ku nyumba yafalitsa nkhani yasindikizidwa, yimbani telefoni. Nyumba zolemba nyuzi zimalandira mazana mazana a kalata zoti zisindikizidwe musabata imodzi. Muyenera kuyesetsa kuti kalata yanu yagwiritsidwa ntchito, chimene chikukuumirizani kuti muimbe matelefoni otsatila kupereka kalatayo. Gwirani ntchito ndi woimilira gululi pochita izi.



Zowonjezera zachiwiri (Annex 2) ndi kalata imene inasindikizidwa mu ndime yoyeselera phunziro limeneli mu dziko la Ireland. Cholinga chake ndikukupatsani maganizo ena ndi chilimbikitso polemba kalata yanu.

Chidziwitso

Cholinga cha kalata imene gulu lanu latulutsa ndi kuti ikasindikizidwe ngati nkhani ya mu nyuzipepala ya mudera lanu. Ngati yasindikizidwa, lembani kalata yothokoza kwa mkozi ndipo itumizeni mofulumira nyuziyi ikangotuluka. Pambuyo pake lilimbikitseni gululi kuti liitanitse mkonzi kapena mtolankhani wa nyuziyi kuti adzamuthokoze pamaso ndikumufunsa ngati pali zinthu zina kapena nkhani zina zoti angazikonde ndi cholinga chakuti nkhani ya m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana ipitilre kukhala mu nyuzi. Kusindikizidwa kwa nkhani yanu mu nyuzi ndi chinthu chopambana kwambiri pa ntchito yanu yozindikiritsa anthu amudera lanu za zomwe zikuchitika. Liuzeni gulu lanu kuti liduleko pepala limene pali nkhaniiyi ndipo atsekule failo momwe angamasungire zinthu ngati izi.

Ngati nkhani yanu siinasindikizidwe, osataya mtima, ndipo onetsetsani kuti gululi lisakhumudwe. Athandizeni polankhula ndi mkonzi kapena mtolankhani kuti mumve chifukwa chimene nkhaniiyi siinatulukire. Iyi ndi ntchito yofunika kwambiri chifukwa mwina pakhonzha ukhala chifukwa chomveka bwino, mwachitsanzo, mwina malo sanali okwanira munyuziyi ndipo kuti ikhonza kusindikizidwa sabata yotsatira. Pofunsa chifukwa chimene nkhani siinatulukire, inu ndi gulu lanu mudzadzziwa chimene chikhonza kuchitika pofuna kuonetsetsa kuti nkhani ina imene mungatulutse ikhale yabwino kuposa imene sinatulukeyi. Inu ndi gulu lanu mungathe kuphunzira zambiri pochita izi ndipo zidzakulimbikitsani powona kuti chinachake chalembedwa mu nyuzipepala chokhudzana ndi m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana komanso zomwe zikuchitika pofuna kuthetsa mkhalidwewu.

Zoyenera kuchita ndi Zoyenera kupewa

- Onetsetsani kuti aliyense akutenga nawo mbali pazochitika zili zonse za chigawo ichi
- Onetsetsani kuti gulu lililonse lalemba kenakake, kangafupike kapena kuchepa mumaganizo.
- Gwiritsani ntchito nthabwala pofuna kuthandiza gululi. Nthabwala zikhonza kugwiritsidwa ntchito pofuna-funa mitu ya nkhani zathu, mwachitsanzo.
- Limbikitsani magulu anu kuti awerenge mokweza makalata awo omwe alemba.
- Yamikirani magulu pa ntchito yawo. Auzeni kuti ntchito yawo idzakhala yoyamikika ngati akwaniritsa kulemba kalata yomaliza yopita ku nyumba yofalitsa nkhani kuti ikasindikizidwe.
- Sungani makalata onse omwe maguluwa atulutsa.



Kukambirana komaliza

Phunziro limodzi

Kugwira ntchito ndi atolankhani ndi chinthu chosangalatsa ndipo gulu lanu lidzakondwa kwambiri ndi zochitika za mu gawo limeneli. Adzakondwa pozindikira kuti anthu a mudera lawo awerenga zimene iwo akuphunzira komanso kuchita. Adzakondwa poona zithunzi zawo ndi za anzawo mu nyuzi. Adzasangalala kuona momwe akuonekera ndikulakalaka kuti anthu owadziwa asaone zithunzizi, koma pansi pa mtima adzakhala osangalala ndi onyadira, ndipo ayeneradi kutero. Aloleni kuti amasuke ndi kuchotsa mantha omwe anali nawo polankhula zakukhosi kwawo zokhudzana ndi ntchitoyi.

Pomaliza alankhuleni mowasangalatsa ndi kuwalimbikitsa. Auzenionse kuti atchere maso pa nyuzipepala yotsatira yamudera lawo kuti awone ngati nkhani yawo ituluke. Ndichinthu chimene aliyense angayembekezere kuti aone ndipo chidzapereka chilakolako chochuluka choti mutsatirensa nkhaniyi. Mwachitsanzo mkonzi akhonza kukhala ndi chidwi chapadela pa nkhani kapena pulojekiti imene mukuchita. Nyumba yolembe nkhani ikhonza kuganiza zolembe nkhani zanu mu nyuzipepala kwa masabata angapo. Mukhonza kuwaunikira kuti ngati angafune angathe kusindikizanso zina mwa nkhani zifupizifupi zimene gululi linalembe kapena ntchito zina za luso zimene gululi latulutsa, mwachitsanzo zithunzi kapena zojambula ndi makaka.



Kuunika momwe ntchito yayendera ndi kuchita kalondolondo

Pa nkhani yowunika momwe ntchito yayendera muchigawo ichi, pali zotsatira zodziwika bwino zoti zikhonza kuwunikidwa kuti muone ngati mwakwaniritsa zonse zomwe mumafuna kuti zichitike. Mwachitsanzo, magulu ang'onoang'ono ayenera kukhala atatulutsa makalata afupi opita ku nyumba yofalitsa nkhani ndipo pogwiritsa ntchito izi, ayenera kukhala atalemba kalata yotalikirapo yolembedwa ndi gulu lonseyo mwe idzasindikizidwe. Zizindikiro zina ndizo:

- Kuti mwadziwana komanso kukumana ndi lemba ndi kufalitsa nkhani a mudera lanu.
- Kuti kalata yachidziwitso yatumizidwa.
- Kuti nkhani yokhudza kalata yachidziwitso yasindikizidwa.
- Kuti ntchito zonse zofunika zayambika kutsatira kusindikizidwa kwa nkhani yanu.

Cholinga cha chigawo ichi ndikukonzekera kuyamba kuchitapo kanthu pa nkondo ya dziko lonse yolimbana ndi m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana ang'ono. Zizindikiro zili m'mwambazi ndizofunika kwambiri pofuna kudziwa momwe gulu lanu likudziperekera potengapo mbali pa nkhaniyi ndi pa pulojekitiyi. Zotsatira za ntchito iyi zidzakhala zofunika kwa inu alangizi, pofuna kudziyesa nokha pa momwe mwagwiritsira ntchito zigawozi kufikira pano. Ndi zothandizanso powunika ngati aliyense mu gulu lanu watengapo mbali pa zochitikazi. Pofika apa muyenera kukhala mutadziwa anthu amene ali odzipereka kwambiri pa zochitikazi.



Mwapadera, chigawo ichi ndichofunikanso ku maphunziro a gulu la achinyamata pa zifukwa izi:

1. Zochitika za muchigawochi ziwaonetsa momwe angachitire kanthu polimbikitsa kuzindikilitsa za vuto lolemba ana ntchito.
2. Akhonza kufotokoza maganizo awo kwa anthu ambiri a mu dela lawo ndiponso kumadela ena akutali.
3. Magulu ena ndi anthu ena akhonza kuonetsa chidwi ndikuyamba kulankhula awo pa zimene akuchita.
4. Oyang'anira maphunziro mu dela lanu akhonza kukhala ndi chidwi ndi zomwe achinyamatawa akuchita.
5. Kufalitsa uthenga kudzera ku nyumba zofalitsa uthenga zikhonza kutsekula makomo ambiri.

Mu chigawochi muli uthenga wachilimbikitso kwa gululi ngati zonse zitatsatidwa ndikugwiritsidwa ntchito bwino. Ngati kalata yanu achidziwitso yasindikizidwa, onetsetsani kuti gulu likulimbikitsidwa ukhala lodzidalira komanso ndi chidwi chochitapo kanthu pa nkhani yogwiritsa ntchito ana ang'ono.

Pamene mwatsiriza chigawo ichi ndipo mwakhutitsidwa, mungathe kupitiriza zochitachita zanu podzera ku nyumba zofafalitsa nkhani (onani "Kufalitsa Nkhani: Pa Wailesi ndi Wailesi yakanema Television). Kalata yopita ku nyumba yofalitsa nkhani imene mwatulutsa idzakhalanso yofunika polimbikitsa ubale ndi nyumba zofalitsa nkhanizi.

Gawo Ioyamba la zowonjezera

(Annex 1)

Nkhani yomwe inasindikizidwa mu
Scariff News, Ireland, March 2001

Mchitidwe Ogwiritsa Ntchito Ana Ang'ono

Olemba: Antoinette Collins (16) ndi Denise Bolton (16)

Mwina mukudziwa kale za pulojekiti ya m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana ang'ono yomwe ife, ophunzira a ku Scariff Community College, tikuchita. Iyi yakhala pulojekiti yotithandiza kudziwa zinthu zambiri. Tapeza ambiri za nkhanza zokhudzana ndi m'chitidwe ogwiritsa ana ntchito komanso zifukwa zimene ana amapezeka ku malo antchito. Tinayamba pulojekiti yathu ngati masewera pamene aliyense anatenga pepala ndi magazini (magazine) akale ndikuyamba kudula zithunzi ndi kupanga chithunzi cha zomatamata. Mu chithunzi choyamba tinasankha tokha zomwe timafuna kuwonetsa.

Chachiwiri chinali chokhudza m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana. Panopa tili nazo zonsezi ndipo tinazipachika muzipupa za mu kalasi yathu. Pa maphunziro athu timakumana kawiri kapena katatu pa sabata ililonse ya pulojekiti yokhudzana ndi m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana ang'ono. Pamisonkhanoyitimakambirana zokhudza m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana. Zina mwa zomwe timaphunzira mu kalasi zikujambulidwa pa kanema ya video ndipo zojambulazi zidzakonzedwa bwino kuti zikhale pulojekiti yapadera ya kanema. Komanso kamodzi pasabata iliyonse, pamene tikuphunzira chingelezi, timawerenga nyuzipepala kuti tione ngati muli nkhanu zomwe zingatisangalatse. Aphunzitsi ena angapo akutengapo mbali pa pulojekiti yathuyi. Panthawi yophunzirayi, timakambirana mitu imene ikukhudzana ndi pulojekiti yathu monga ngati mu phunziro la ***zachilengedwe ndi nyengo (geography)*** momwe tikuphunziramo zina mwa zimene zimayambitsa umphawi.

Dera lina la pulojekiti yathu, limene tonse tikulikonda ndi a zisudzo. Phunziro limeneli ndilosiyana ndi zimene ena a ife tinachitako. Panopa tikukonzekera sewero la chigawo cha achinyamata lokhudzana ndi msonkhano wa magulu a zisudzo pa 15 March. Pa 14 February tinachita mtsutso. Mutu wake unali, "Ana ayenera kukhala ku sukulu osati ku malo a ntchito". Izi zinali zothandiza potidziwitsa zinthu zina.

A khansala a dela la Clare County anadzaonelera mtsutsowu ndipo anatiuza za momwe anakhudzidwira ndi zolankhula zathu. Phungu wa nyumba ya malamulo amene anadzatiyenderanso anakhutitsidwa ndi pulojekiti yathu. Ophunzira angapo anafunsa mafunso kwa anthu a ndalewa.

Kuyambira pa 15 kufikira pa 16 February tinali ndi maphunziro osangalatsa okhudzana ndikulemba za msangulutso amene anachititsa ndi katswiri olemba Larry O'Loughlin. Larry analemba buku akuti “Kodi alipo akumvetsera? Bukuli limakamba za m’chitidwe ogwiritsa ntchito ana. Aliyense anakondwa ndi kubwera kwake.

Pulojekiti yathu ndiyokhudza achinyamata ndi zimene tingachite kuti tithetse m’chitidwe ogwiritsa ana ntchito padziko lonse. Pokambirana zambiri za mavutowa ndikumvetsetsa chifukwa chimene izi zimachitikira, tikuona kuti tikhonza kutengako mbali pochitako kenakake pa vutoli. Munthu akazindikira zimenezi, ndikosatheka kuti angakhale phee osachitapo kanthu.

Pogwiritsa ntchito luso limene taphunzira, tikukhulupilira kuti tikhonza kubweretsa kusintha. Choncho pulojekiti yathu ikufuna kubweretsa kusintha ku miyoyo ya miyandamiyanda ya ana ang'ono amene akugwira ntchito pa dziko lonse lapansi.

Gawo lachiwiri la zowonjezera

Kalata yolembedwa ndi gulu la ku Ireland,
Mwezi wa January 2001

Ntchito ya Chikondi ya Ophunzira a ku Scariff

Gulu la achinyamata ochokera ku Scariff Community College akutsogolera pulojekiti yosiyana ndi mapulojekiti ena onse imene ikhonza kuthandiza pothetsa mtundu oipitsitsa wa m'chitidwe ogwiritsa ana ntchito pa dziko lonse. Ophunzira 24 a ku East Clare Secondary School akutenga mbali popanga pologalamu yongoyesera yomwe cholinga chake ndikudziwitsa achinyamata pa nkhani zokhudzana ndi m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana.

Moyang'aniridwa ndi bungwe loyang'anira anthu ogwira ntchito pa dziko lonse lapansi (ILO) ku Geneva, Switzerland, pulojekitiyi ikukonzedwa ndi bungwe la Pologalamu yothetsa m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana padziko lonse lapansi (IPEC). Iwo analemba ntchito a Nick Grisewood, katswiri (odziyimira pa yekha) pa ntchito yofalitsa mau amene amakhala ku Cardiff, kuti akonze mabuku a maphunziro amene angathe kugwiritsidwa ntchito mu sukulu za dziko lapansi.

Chinthu chimene chikubweretsa zinthu za chilendo mu pulojekitiyi ndi chakuti ikukhudza madera onse azimene ophunzira ayenera kuphunzira monga momwe akufotokozera Geraldine Condren, ophunzira owongolera zochitika za ophunzira onse a Form 2. "Ophunzira akuunika nkhani ya m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana kuchokera ku mfundo zosiyanasiyana..... akupanga zithunzi zopachika pa chipupa mu kalasi yawo ya zaluso, akuphunzira za nkhani ya umphawi kudzera mu phunziro la geography, akuunika ndakatulo ndi nkhani zogwirizana ndi m'chitidwewu pophunzira zilankhulo za ku Ireland ndi chingezezi ndipo anakonzanso mtsutso okhudzana ndi nkhanayi kumene kunabwera ophunzira a pa sukuluyi".

Polojekitiyi imadalira kwambiri kugwiritsa ntchito zisudzo, nyimbo ndi kulemba nkhani za msangulutso. Ophunzirawa akugwira ntchito ndi okonza zisudzo wa mudera lawo kuti akonze sewero limene lidzaphatikizidwe pa msonkhano wa ochita zisudzo wa chaka chino umene ukachitikire ku Clare.

Anthu a mudera limeneli tayilandira bwino kwambiri nkhaniyi. Nyumba yosungira ndi kubwereketsa mabuku m'dera la Clare yathandiza popereka maphunziro akagwiritsidwe ka makina a **(Internet)** ndi mwayi ogwiritsa ntchito makinawa kwa ophunzira amene akutenga mbali pa nkhaniyi komanso nyumbayi yapereka zipangizo zochitira kafukufuku mu nyumba zosungira ndikubwereketsa mabuku za Killaloe ndi Scariff.

Tikukhulupirira kuti kusintha kwina kulikonse pa nkhani ya m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana padziko lonse la pansi kungatheke ngati atsogoleri a ndale atengapo mbali. Polingalira zimenezi ophunzirawa anayitanitsa a ony Killeen TD ndi a Paul Bugler kuti adzacheze ku Scariff Community College ndi kuti adzaone okha zomwe zikuchitika. Zotsatira zake ndi zakuti atsogoleri onsewa analonjeza kuti achitapo kanthumu dera lawo komanso mu dziko lonse pofuna kupititsa patsogolo ntchito yodziwitsa anthu za nkhaniyi.

"Kudzipereka ndi chidwi cha ophunzirawa ndi chilimbikitso choposa zonse kwa anthu ogwira ntchito ku IPEC ku Geneva ndi dziko lonse lapansi" akutero Frans Roselears, wamkulu wa IPEC ku Geneva. "Tikukhulupirira kuti achinyamata akhonza kutsogolera pobweretsa kusintha ngati luso lawo lopeka ndikuganizira za mavutowa litalimbikitsidwa. Choncho aphunzitsi ayenera kulimbikitsa luso la achinyamatawa kuti athe kutenga maudindo pomanga chikhalidwe cholemekeza ufulu wa anthu".

Kumapeto kwa zonse, kupambana kwa pulojekiti ya Scariff Community College kudzaoneka powunika momwe ophunzira aku East Clare angakwaniritsire kudziwitsa anthu za nkhaniyi. Ophunzira wina Nollaig Burke akufotokoza: "Pali chiyerekezo chakuti kuli ana oposa 245 miliyoni azaka zosakwana 18 amene akugwira ntchito padziko lonse. Mwa amenewa, pafupifupi 179 miliyoni akugwira ntchito munjira zoyipitsitsa mu m'chitidwe ogwiritsa ntchito ana. Pulojekiti yathu ifikira dziko lonse lapansi kuthandiza kuphunzitsa achinyamata ena zazoopsya zimene ana ena akukumana nazo. Ndiuthenga umenewu, ndikhulupilira kuti, iwo ndi ife, tikhonza kubweretsa kusintha kokhazikika" IPEC inakhazikitsidwa m'chaka cha 1992 kuti ithandize maiko kuti alimbane ndi m'chitidwe ogwiritsa ana ntchito kudzera mu zochitika za mu mapologalamuwa, kafukufuku ndi kukonza mfundo zoyendetsera zochitikazi, komanso kumenyera ufulu. IPEC tsopano ikugwira ntchito mu maiko 74 muzigawo zonse za dziko lapansi.



Lekani Kugwiritisa Ntchito Ana

ILO

International programme on the
Elimination of Child Labour (IPEC)

ILO/ IPEC Malawi Project
Mantino Complex
Behind Bizonowaty filling station
PO BOX 30135
Lilongwe

Tel: (+265)-0- 1 770 388/ 199/155

www.ilo.org/ipec

ISBN 92-2-113240-4

